Yesu anayankha kuti, "Ine ndiye njira, choonadi ndi moyo. Palibe munthu angafike kwa Atate popanda kudzera mwa Ine."

— Yohane 14:1–6

Ukali opanda chifundo

"Ukali Opanda Chifundo" ndi m'mene Billy Machilika akudzifotokozera za khalidwe lake la ukali pamene ankasuta Chamba. "Ndinkasuta mpaka zaka zambiri," Billy akufotokoza, "Sindinali munthu wa mtendere koma akusowetsa mtendere ndipo anthu ambiri amasowa mtendere chifukwa cha khalidwe langa loipa mtima loyambitsidwa ndikasuta chamba."

Billy anabadwa tsiku la Christmas mu chaka cha 1984 ku Blantyre, Malawi. Iye anakulira kumeneko asanabwere ku Zomba. Ndi

zomvetsa chisoni anali mu goli losuta chamba pamene amafuna kupeza mtendere m'maganizo. Iye akuti, "Kupanda kusuta ndinalibe mpumulo. Ndimapeza mtendere wa kanthawi, koma wabodza ndikasuta."

"Ndimamwanso mowa zedi, ndimakhaliwa m'malo omwera mowa. Machimo enanso (kuchita ndi kuganiza zoipa) zinayambanso kuonekera chifukwa cha kuledzera kwanga." Billy anafotokoza za kuwawa kumene mkhalidwe wake wa chiwerewere unabweretsa kwa akazi amene anali nawo mu maubwenzi ndipo makamaka mkazi wake komanso ana. Iye akukumbukira, "Ndimatha ngakhale kutuma mkazi wanga kukandigulira chamba." Iye samakhudzika kuti zimenezi zimabweretsanso mavuto akulu kwa makolo a mkazi wake.

Billy akuvomereza, "Mkazi wanga ndi ana amazunzika, kumva kuwawa chifukwa cha mkhalidwe wanga oipa umenanso unasokoneza (maphunziro a ana) ndi madera ena m'miyoyo yawo, chifukwa ndalama zimene ndimapeza zimakathera ku mowa ndi akazi."

Billy akuvomereza zoipa zambiri m'moyo wake. "Ndimakonda kumuza mkazi wanga kuti sitingapange bizinesi popanda mankhwala a

kwa sing'anga. Timadzicheka ndi malezala m'matupi mwathu kuti tithire mankhwala amene cholinga chake chinali kuti tidzipeza phindu ku bizinesi komanso chitetezo ku ndalama zathu." Tsiku lina mu chaka cha 2020 Billy anamva choonadi chokhudza iye mwini ndipo zinamusowetsa mtendere zedi. Munthu wina anamufotokoza za chimene uchimo uli—monga m'mene Baibulo limafotokoza.

Munthu ameneyo amalalikira kuchokera pa Agalatiya mutu 5 ndime 19 mpaka 21, imene imati, "Ndipo ntchito za thupi zionekera, ndizo dama, chodetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kuduka, zopsya mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mchezo, ndi zina zotere; zimene ndikuchenjezani nazo, monga ndachita, kuti iwo akuchitachita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu."

Billy anazindikira kuti iye anali kapolo weniweni wa uchimo ndipo kuti anali opandiratu mphamvu kudzikana kupanga choipa, kapena kusintha njira zake. Komanso anayamba kuopa imfa ndi kumakhala ndi maloto a imfa yake yomwe.

Mu mwezi wa November pa 20, chaka cha 2020 iye anaganiza zochita chinachake chokhudza bvuto limeneli. "Ndinali wotsutsika chifukwa cha moyo wanga wa uchimo, ndipo ndinapita ku malo amene munthu amene amandiuza za uthenga wabwinoyo

amakumana ndi anzake otembenuka mtima. Uthenga unalalikidwa umene umalunjika za moyo wanga wauchimo komanso m'mene ndinalili osatha kudzisinthana ndekha moyo wanga popanda Kristu." Billy anamvetsetsa choonadi ndipo anazindikira kuti

Yesu Kristu anali ndi mphamvu kumusintha iye komanso kumukhululukira iye zolakwa zake zonse—ndi kumuthandiza komanso kumatsogolera m'moyo wake wonse!

Pakuika chikhulupiriro chake mwa Yesu, ndi kuvomereza iye ngati Ambuye wake komanso Mpulumutsi, Billy pomwepo anapulumutsidwa kumachimo ake onse! Yesu ali ndi mphamvu yokhululukira machimo chifukwa iye analipira kale ndi mwazi wake chilango cha uchimo. Baibulo limati, "mphotho ya uchimo ndi imfa." (Aroma 6:23)

"Kuyambira tsiku limenelo kulemera mu mtima mwanga komanso m'thupi mwanga zinachoka," akuteru Billy, "ndipo ndinayamba kukhala pa chiyanjano

ndi anthu otembenuka mtima. Koma anzanga akale amati ndinasiya kumwa mowa ndi kusuta chifukwa ndinalibe ndalama! Ena amandilimbikitsa kuti ndiyambirensa ndi kudziikanso mu ukapolo ndekha ndi moyo wanga wakale."

"Ndinawauza kuti, Iye amene ali mwa ine, Mzimu wa Yesu Kristu, ndi okwanira."

Billy wapeza Mpulumutsiyo Yesu Kristu kukhala okhulupirika kwa iye ndipo, "Iye (Yesu Kristu) akupitiriza kukhala Ambuye athu kufikira tsiku la lero," Billy akuchitira umboni.

"Tikhoza kukhala ndi ndalama zochepa ngati banja, koma Kristu ndi zonse mu zonse, ndipo ndi okwanira kwa ife. Mwa Iye timapeza mpumulo wa miyoyo yathu."

Munthu amene anatsala pang'ono kuonongedwa ndi mowa komanso chamba komanso zotsatira zake kunali kusapeza mpumulo, tsopano ali ndi mtendere ndi mpumulo. Iye analibe cholipira kuti apeze moyo uyu watsopano. Inali mphatso yaulere kuchokera kwa Ambuye wake, Yesu Kristu.

"Pakuti pamene inu munali akapolo a uchimo, munali osatumikira chilungamo. Ndipo munali nazo zobala zanzi nthawi ija, m'zinthu zimene muchita nazo manyazi tsopano? pakuti

“

Mkazi wanga ndi ana amazunzika.

”

“

Yesu ali ndi mphamvu yokhululukira machimo

”



chimaliziro cha zinthu izi chili imfa. Koma tsopano, pamene munamasulidwa ku uchimo, ndi kukhala akapolo a Mulungu, muli nacho chobala chanu chakufikira chiweretso, ndi chimaliziro chake

moyo wosatha. Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu." (Aroma 6:20–23, Baibulo)



If you would like to know more about God, systematic study of God's Word (Bible), and grow spiritually, we welcome you to join a free Bible study course

STUDY THE BIBLE WITH EMMAUS CORRESPONDENCE SCHOOL

Over 70 years experience in correspondence ministry; nearly 25 million courses in 128 languages already distributed in more than 100 countries.

Biblically sound & solid! Uncomplicated and straightforward. Flexible studying times – study at your own home, time & pace.

CONTACT:

Blantyre: ECS, PO BOX 31621, Chichiri, Blantyre 3 0885 010 009
Zomba: ECS, PO BOX 768, Zomba 0995 361 850 0888 004 853

EXCELLENT AND WONDERFUL CHRISTIAN BOOKS AVAILABLE WRITTEN BY DR JONATHAN NEWELL

How does the Bible's teaching relate to everyday life in Africa?

Fear on Every Side is a new approach to practical Biblical teaching for everyone who lives and works in Africa. Using the format of a novel, *Fear on Every Side* offers an exciting read. Beautifully illustrated with contemporary photographs, along with challenging discussion questions and Biblical references at the end of every chapter.

The Journey of Life?

The Christian life is like a long journey. Like every journey, it has a beginning and an end. There are people we meet on the way and things that happen, both encouraging and disappointing, joyful and sad, exciting and frightening. This book helps us prepare for what we are going to meet as we walk 'the journey of life.' Available in **Chichewa** also.

The adventures of Blessings Minibus

The adventures of BLESSINGS MINIBUS are designed to help the children of contemporary Africa to understand the parables of Jesus and their messages. Each book has some Bible studies at the end to study Jesus' parables more deeply. **Blessings Minibus and the Journey to South Africa:** One of Blessings' friends goes to South Africa and finds that life there is not as wonderful as he had assumed. **Blessings Minibus and Rules Minibus Patrol:** Rules Minibus Patrol refuses to forgive Blessings for a small bump and so gets into trouble with an Honest Police Land Cruiser.

Available from bookshops and church bookstores throughout Malawi
Contact: 0885 010 009 or write to P.O. Box 31621, Chichiri Blantyre 3
Email: agapemalawi@gmail.com

Moyo Wodabwitsa wa Yesu Kristu

Yesu anaikidwa ndi Mulungu pa utumiki wapadera padziko lino lapansi. Iye amadziwiratu zoti adzachite. Nthawi yamoyo wake pansi pano analalikira ndi kuphunzitsa choonadi cha Mulungu ndi ulamuliro. Anamasula anthu ku ukapolo wa tchimo. Yesu anamaliza cholinga chake pakufa pamtanda chifukwa cha machimo athu. Anatha kuchita zimenezi chifukwa cha chimene iye ndi—yekhayo, Mwana yekhayo wa Mulungu.

Kuwerenga Kwa Mau A Mulungu (Chonde muziwerenge ndimezi):

Mateyu 23:27-33; Marko 2:13; Luka 2:9-14, 22; 5:20; Luka 19:10; Yohane 1:18; 13:1-3; Afilipi 2:7, 8; Aheberi 2:14; 1 Yohane 3:5.

Yesu Kristu ndi Woposa Aliyense, Iye ndi Wopambana

MU mitu yoyambirira ya uthenga wabwino wake, Luka akufunitsitsa kutionetsa kuti Yesu ndi wopambana. Palibenso wofanana naye. Luka akuonetsa izi pakupereka mitundu itatu yokhudza kupambana kwa Yesu.

Mau amene anayankhula Mulungu pa kubadwa kwa Kristu amaonetsa kuti Kristu anali wopambana. Mulungu Tate anatengapo gawo pa kubadwa kwa Yesu. Ambuye Yesu Kristu anabadwa kudzera mwa mphamvu ya Mzimu Woyera (Luka 1:35). Mulungu anagwiritsa ntchito Angelo kuti alosere za kubadwa kwa Kristu kwa Maria, mayi wake (Luka 1:26, 27). Mulungu anatomiza mauthenga kwa anthu kudzera mwa Mzimu Woyera (Luka 1:41, 42, 67; 2:27, 28). Mulungu anatomiza Mngelo ndi woyimba a kumwamba kukayankhula ndi abusa pa zakubadwa kwa Yesu (Luka 2:9-14).

Yesu asanayambe utumiki wake, panali mboni zambiri kuikira umboni kuti Yesu analidi Mau a Mulungu ku dziko la Israeli ndi kuti Iye anali Mpulumutsi wawo wolonjezedwa uja. Yohane Mbatizi anayankhulapo za kubwera kwa Kristu (Luka 3:1-18) monga m'mene Chipangano Chakale chinaloserera. Panalinsu umboni wa mau wochokera kumwamba amene anali mau a Mulungu pa kubatizidwa kwa Kristu (Luka 3:21, 22).

Mbiri ya makolo ake a Kristu monga mwa thupi (Luka 3:23-38) imaonetsa kuti Yesu anayera kupeza m'ndandanda wa banja lake kwa Mfumu Davide. Yesu anali Mfumu yeniyeni ya Israeli. Anayeneranso kupeza mtundu wake kwa Abrahamu, zimene zikuchitira umboni kuti Iye anali Muyuda weniweni.

Kulimbana kwa Yesu ndi Mdyerekezi (Luka 4:1-13) zikuonetsa kuti Yesu ndi wolamulira

Mdyerekezi. Yesu anali ndi mayankho ku mayesero. Iye anabwera kudziko kudzathana ndi Mdyerekezi ndi tchimo (1 Yohane 3:8). Kuyesedwa kwake kunaonetsa kuthekerera kwake.

Luka analamba zinthu zingapo zimene zikuonetsa ulamuliro wa Yesu pa zinthu za moyo uno.

Ulamuliro wa Yesu

- Pa Mizimu Yoipa/Yonyasa — Luka 4:33, 36
- Pa Matenda Onse — Luka 4:38, 40
- Pa Chilengedwe — Luka 5:1, 7
- Pa kuyendetsa Miyoyo ya anthu — Luka 5:8, 11
- Pa kufotokoza ndi kutanthauzira Chilamulo cha Ayuda — Luka 5:33; 6:10

Chinthu china cha moyo wa Yesu, ndi kukhala kwake ndi Mzimu Woyera. Ubale umenewu ukupezeke mu uneneri (Yesaya 11:1, 2; 42:1; 61:1). Zikuonekanso mu kubadwa kwa Yesu (Luka 1:35), moyo wake (Luka 3:22; 4:1, 14 18; Yohane 16:14), imfa yake (Aheberi 9:14), ndi kuuka kwake (Aroma 8:11).

Yesu anakhala mu m'chiyanjano ndi Mzimu Woyera nthawi zonse. Anali wodzala, wodzadza komanso wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera nthawi zonse. Moyo wake unali wodziwika ndi zipatso za Mzimu Woyera. Izi ndi zoonza chifukwa lye anali munthu wangwiro ndiponso mtumiki wa Mulungu wangwiro.

Mu Luka 3:22 tikuwereza za Mzimu Woyera akutsikira pa Yesu ngati nkunda. Izi zizinachitike pofuna kumudzadza ndi Mzimu Woyera, iyai, pakuti lye anali

wodzala, wodzadza kale ndi Mzimu Woyera. Koma kuti, Mulungu anamudzodza, moonekera kumusankha ku utumiki umene anauyamba, izi zitangotha (Machitidwe Atumwi 10:38). Choncho, kutsika kwa Mzimu Woyera pa Yesu unali mwambo umene unachitidwa ndi Atate ndi Mzimu Woyera.

Mbali yaikulu ya ntchito ya Yesu pa dziko lino lapansi inali kuphunzitsa za Mulungu. Mauthenga abwino ndi odzadza ndi nkhani zokhudza ziphunzitso zake, kuphunzitsa makamu a anthu (Marko 2:13), kuphunzitsa kagulu kakang'ono ka ophunzira ake (Yohane 13:3-10), komanso kuphunzitsa munthu m'modzimidzi

(Yohane 3:2-3; 4:9-10). Mbali yaikulu ya Mauthenga abwino yalemba ziphunzitso zake monga Chiphunzitso cha pa phiri (Mateyu mitu 5 mpaka 7), chiphunzitso cha pa phwando la pa Paska (Yohane 13-16), ndi uthenga wake okhudzana

ndi zozizwitsa komanso zizindikiro (Yohane 5-7).

Mu ziphunzitso za Yesu, mu Mauthenga onse abwino tikuona kuthekerera kwake ngati mphunzitsi. Anaphunzitsa m'mafanizo, miyambi, imene ili nkhani zosavuta kumvetsa zoti ngakhale ndi ana omwe angamvetse, koma mafanizowa amakhala ndi matanthauzo ozama.

Yesu anaphunzitsa ndi ulamuliro. Iye samangobwereza zimene anthu ena ananena kale m'kumauzanso ena zomwezo. Unali muyeso wa Chiyuda kunena kuti, "Rabbi, Mphunzitsi wakuti-wakuti ananena izi ... " Mosiyaniitsa, Yesu anaphunzitsa, "Koma ine, ndikunena kwa inu ... " (Mateyu 5:21, 22). Iye anayankhula ndi ulamuliro umene anthu anazizwa nawo (Mateyu 7:28, 29).

Ziphunzitso za Yesu zinali za mkhalidwe wapamwamba kwambiri kuposa aphunzitsi a nthawi yake. Mwachitsanzo, lye anaphunzitsa anthu kuti azikonda adani awo. Yesu anafotokoza choonadi chimene sichinadziwika

Muloweze ndime izi m'mtima mwanu:
Luka 4:18-19, Yesu anati,
 "Mzimu wa Ambuye uli pa lne, chifukwa chake lye anandidzoza lne ndiuzi anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma lne kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyanso, kutulutsa ndi ufulu ophwanyika, kulalikira chaka chosankhika cha Ambuye."

KUPHUNZIRA MALEMBO OYERA

WOLEMBA: JOHN FINEGAN

Mkusindikiza kwa Nyuzipepala iyi ya Challenge Newspaper, tili ndi gawo lachisanu za maphunziro kuchokera m'Buku Lopatulika. Timaphunzira zosiyana zokhudza Yesu Kristu. Tikufunsa, "Kodi Kristu Ndi Ndani?" Cholinga chake ndi chakuti inuyo, owerenga, mudzilimbikitsidwa pakuwerenga choonadi chopezeka m'Baibulo, komanso kulimbikitsidwa kuwerenga Baibulo pa inu nokha. Mu mkusindikiza kwa Nyuzipepalayi kukubweraku maphunziro ena atsopano. Mulungu amalankhula nafe kudzera m'Mau ake, Malembo Oyera. Ndi chinthu chabwino kuti tidzakhale ndi nthawi ya kuwerenga zimene Mulungu akufuna kuti atiuze kudzera m'Mau ake. Izi ndi zofunikira kwambiri kuposa kumva uthenga kuchokera kwa alaliki ngakhaleenso ziphunzitso za zipembedzo.

ndi kale lonse. Mu Luka 16:19-31 Yesu anafotokoza za moyo wina munthu akamwalira, zimene zinali zoti zizinafotokozeredwe lye asanabwere.

Mau a Yesu anali a chifundo, chisomo ndi a chikhululukulo (Luka 4:22) komanso amaulula ku samalitsa kwake. Komabe, podzudzula mizimu yoipa amayankhula ndi mphamvu ndi mwachindunji (Mateyu 23:27-33).

Mau ake anali okhalitsa ndi opindulitsa. Mau ake sadzatha (Mateyu 24:35). Mau ake amabweretsa moyo wosatha (Yohane 6:63, 68) ndipo mauwo ndi muyezo umene anthu adzaweruzidira (Yohane 12:48).

Cholinga cha Kubwera Kwa Yesu pa Dziko Lapansi

Yesu anali ndi zifukwa zenizeni zokhalira munthu ndi kukhala padziko lino lapansi.

1. Iye anabwera ndi cholinga cha kudzakhala nafe ndi kukhala munthu ngati ife (Mateyu 1:23; Aheberi 2:14). Yesu anali ndi thupi komanso mwazi ngati ife.
2. Kubwera kwake lye anachita utumiki kukwaniritsa cholinga cha Mulungu (Afilipi 2:7, 8; Aheberi 10:5-7).
3. Kubwera kwake kunapangitsa lye kukhazikitsa chitsanzo kwa ife cha

moyo wa umulungu (1 Yohane 2:6).

4. Iye anabwera kudzaphunzitsa choonadi cha uzimu ndi kusamalira osowa (Luka 4:18).
5. Anabwera ndi cholinga chodzaonetsera Mulungu mwa lye (Yohane 14:9).
6. Yesu anabwera kudzaononga Mdyerekezi ndi ntchito zake (Aheberi 2:14). Kristu ndi chigonjetso chathu tsopano!
7. Iye anabwera ndi cholinga chodzadziwa m'mene moyo wathu umakhalira ndi kumva nafe chifundo ndi mavuto athu (Aheberi 2:17), 18; 4:15).
8. Kubwera kwake lye anakhazikitsa banja latsopano la anthu pakuwapatsa iwo moyo ndi kuwalungamitsa (Aroma 5:12-21).
9. Iye anabwera ndi cholinga chodzatifera ife chifukwa cha machimo athu ndi kupereka njira imene Mulungu angatikhululukire machimo athu (1 Yohane 3:5). Ndi Yesu yekha amene akanatifera ife, pakuti lye ndi wopanda tchimo.

Phunziro ili, kuchokera m'Buku Lopatulika, lidzapitirira mkusindikiza kwa Nyuzipepalayi kukubweraku, tikadzaona Maphunziro ena atsopano.

MUDZIYESE!


Tiyeni tilingilirebe za zonse zimene tawerenga m'phunziroli. M'munsi muno muli ndime anayi. Mawu ake a ndime zina ndi zoonza, koma ena ndi mabodza. Mutawerenga phunziro ili, werengani ndime yoyamba m'munsi. Mukatsimikiza kuti mawu ake akugwirizana ndi Phunziroli, lembani **ZOONA** patsogolo pake. Ngati sakugwirizana, lembani **MABODZA** patsogolo pake. Mukachita choncho, lembani **ZOONA** kapena **BODZA** patsogolo pandime ili yonse.

1. Kulimbana kwa Yesu ndi Satana (Luka 4:1-13) zikuonetsa kuti Satana ndi wofanana ndi Kristu m'mphamvu. _____
2. Luka 3:22 akufotokoza kuti Mzimu Woyera anatsikira pa Iye akuoneka ngati nkunda. Izi zinachitika ndi cholinga cha kudzodza Yesu, moonekera, ku utumiki Wake. _____
3. Mbali yaikulu ya ntchito ya Yesu pa dziko lino lapansi inali kudzakhala moyo wosalakwa. _____
4. Luka akutsatira za makolo a Yesu kuchokera kwa Ayuda ofunikira awiri ati Mose ndi Abrahamu. _____

Mutamaliza kuyankha mafunso onse, mungadziyese popeza mayankho enieni analembedwa munsi muno:

MAVANKHO : 1. Bodza, onaninsu Luka 4:1-13; 2. Zoona, Luka 3:22; 3. Bodza, Iye amaphunzitsa zokhudza Mulungu; 4. Bodza, Abrahamu ndi Davide, werengani Luka 3:23-38.

POWER OF THE CROSS A Joyful 'toon by Mike Waters



For the message of the cross is foolishness to those who are perishing, but to us who are being saved it is the power of God. - 1 CORINTHIANS 1:18 NIV

SUBGROUP	Y	9	7	6	2	3	4	5	8	1
I	I	A	A	E	8	2	5	6	7	1
N	A	P	E	T	I	R	A	N	A	4
G	L	S	S	R	4	1	3	5	8	9
A	G	A	P	E	I	N	P	U	T	1
P	N	A	I	F	H	2	5	9	8	4
O	B	E	I	S	P	E	A	R	7	3
R	R	I	N	I	7	3	8	1	9	6
E	N	T	O	M	B	K	N	O	T	3
A	L	I	I	I	5	9	7	4	1	3
N	L	A	S	V	E	G	A	S	6	8

Christian Atsu of Newcastle United runs with the ball during the Premier League 2 match between Leeds United and Newcastle United at Thorp Arch Training Ground on March 15, 2021 in Leeds, England. (Photo by Serena Taylor/Newcastle United via Getty Images)

INSET: Christian Atsu. (Getty Images)



Leaving a lasting legacy

Rising from abject poverty in Ghana, Christian Atsu played for English soccer teams in Chelsea, Everton, Bournemouth and Newcastle before being signed to Turkish club, Hatayspor in 2022.

Tragically it was there that he lost his life in the earthquake in 2023, aged only 31. He left behind his wife, Marie-Claire Rupio, and two sons and a daughter. He also left behind a legacy of strong faith in Jesus.

“My faith is the most important thing in my life,” he told The Guardian. “I know I’m one of the lucky people God has blessed. I’m very lucky and privileged to be in such a position. I had nothing and

now I’ve got so much I have to give something back.”

Christian was a young teenager when he made the decision to follow Jesus for himself.

“I reached a level where my parents didn’t have to tell me I have to go to church, or do this or do that,” Christian said in an article for the Newcastle United website. “I realised that I have to make the choice. Parents don’t force their children to go to church. They make sure they bring you up in the way of the Lord, and then you make the decision yourself. That’s what I did.”

Following his death, tributes flowed in from around the world for the winger, who was once hailed as

the Ghanaian Messi.

His body lay in state for a week before his funeral, which included a military procession. He was buried in his hometown, Dogobome in Ada Foah, on Ghana’s south east coast.

Christian’s professional career began with Portuguese team FC Porto when he was 17. Two years later he joined Chelsea on a five-year contract and was immediately loaned to Dutch club Vitesse Arnhem, followed by Everton, Bournemouth and Málaga. Christian joined Newcastle United in 2016, where he stayed until 2021. He then joined Al Raed Saudi Football Club.

In September 2022, he joined Turkish professional league Süper Lig’s club Hatayspor. He played three league games and one in the Turkish Cup. The day before the earthquake, Christian scored the only goal at home to Kasimpasa in the seventh minute of added time.

He represented Ghana at the 2014 FIFA World Cup and four Africa Cup of Nations tournaments. His team was the runner-up at the 2015 Africa Cup of Nations, where he was awarded Player of the Tournament and Goal of the Tournament.

Despite Christian’s international success, however, he never forgot his roots or his family back home. “Whenever I go home, I am happy,” he told Arms Around the Child, for whom he was a global ambassador. “You never forget the person you were before you left. I survived but I don’t forget.”

He was one of 10 siblings and was only 12 when his father died. Just before his father died, he told Christian that he should worship God and help humanity.

Growing up in poverty was not easy for Christian, however and he found it hard to accept the cards he had been dealt.

“Sometimes I would complain to God a lot: ‘Why should I suffer like this? Why should some people have it easy?’ When I was growing, I would read the Bible, trying to understand everything. ‘Why?

Why? Why?’

“Then I realised that I was complaining too much. God’s power has to be manifested in my life for people to see how far He has brought me. The Bible says it is not by our hard work, by what we do, that makes us reach the level that we are now. For example, like me – it is not just by my hard work, though I am working hard, but it is the will of God, the grace of God, that has brought me this far.”

While in England, Christian attended church in Newcastle, stating that he was there to worship

God and enjoy the freedom it gave him.

“In the house of God I’m normal,” he said. “I don’t want a celebrity life. When I feel normal I feel free.”

After Christian’s death, former West Ham and Fulham defender John Paintsil paid tribute to his friend. “He helped a lot of people solve their problems, gave out to those in need,” he told BBC Ghana.

Despite his sports success, Ghana’s news outlets claimed that 95 percent of tributes about Christian were focused on his humanitarian work such as bailing out Ghanaians who had been jailed for stealing food.



Ghanaian soccer player Christian Atsu’s wife Marie-Claire Rupio (L) and children at his funeral at the State House in Accra, Ghana on March 17, 2023. (Photo by Kwame Adzaho-Amenortor/Anadolu Agency via Getty Images)

Could God love someone like me?

Kodi Mulungu angathe kukonda munthu ngati ine?

The Bible says: “... if you confess with your mouth the Lord Jesus and believe in your heart that God has raised Him from the dead, you will be saved.” (Romans 10:9)

The Bible also says: “Yet to all who received Him, to those who believed in His name, He gave the right to become children of God.” (John 1:12)

If you would like more advice about spiritual matters or more information about Challenge - The Good News Paper (Malawi Edition) please write to (see address below):

Kodi Mulungu angathe kukonda munthu ngati ine?

Mau a Mulungu akuti: “... ngati uvomereza ndi pakamwa pako kuti Yesu ndi Ambuye, ndipo ukhulupirira mumtima mwako Mulungu adamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka.” (Roma 10:9)

Mau a Mulungu akutinso: “Koma onse amene anamlandira lye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu akukhulupirira dzina lake.” (Yohane 1:12).

Ngati mufuna kulandira malangizo apadera okhudza zauzimu kapena ngati mufuna kudziwa za mbiri za Challenge - The Good News Paper (Malawi Edition) lemberani ku:

CHALLENGE MALAWI

P.O. Box 31621 Chichiri Blantyre 3

Phone 0885 010 009

Email: challenge_mw@gmail.com www.challengenews.org/mw

DISTRIBUTED BY: